
THE BOOK OF JONAH (CHINYANJA)
PUBLISHED BY THE BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P.O. BOX 31995, LUSAKA, ZAMBIA

File 1982

# BUKU LA YONA



# BUKU
# LA
# YONA

W.M.U. PROGRAMMES
(CHINYANJA)

FIRST PUBLISHED
JANUARY 1, 1982

BY THE
BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P.O. BOX 31995
LUSAKA, ZAMBIA

KUTSIRIZA:

Mulungu amatilonjeza nzeru. Iye amatilonjeza Mzimu Woyera kuti atiphunzitse. Iye amatilonjeza kutipatsa mphamvu. Iye amatilonjeza kutipatsa zipatso ndikuti adzakhala nafe nthawi zonse. Tiyeni tidzipereke tokha kuutumiki wace, podziwa kuti iye adzatipatsa zosowa zathu zonse.

PEMPHERO:



**MNDANDANDA WA W.M.U.**

PHUNZIRO    MUTU 1: BUKU LA YONA    TSAMBA


1. YONA-ATHAWA KWA MULUNGU..............1

2. YONA-ATHAMANGA NDI MULUNGU............6

3. YONA-ATHAMANGA PATSOGOLO PA MULUNGU..11

MUTU 2: KODI CINGATISIYANITSE NDI CIANI KU CIKONDI CA KRISTU.

4. KUKOMANA NDI IMFA WOSAOPA............16

5. ZOKHUMUDWITSA MBANJA CIFUKWA COSABALA ANA KAPENA KUKHALA NDI AMBALI IMODZI..............................20

6. KUIMA MOLIMBIKA MCIKHULUPIRIRO KUPYOLERA MMABVUTO...................25

7. KUKOMANA NDI ZOKHUMUDWITSA NDI CIKHULUPIRIRO........................29

MUTU 3: MALONJEZO A MULUNGU

8. MALONJEZO A MOYO WOSATHA.............34

9. MALONJEZO AZA MAPEMPHERO.............39

10. MALONJEZO ONENA ZA MADANDAULO NDI MAYESERO............................44

11. MALONJEZO ONENA ZA NZERU MPHAMVU NDI UTUMIKI.........................49

pakucita zabwino, pakuti pa nyengo yace tidzatuta tikapanda kufoka" (Agalatiya 6:9). Munthu amene amapereka umboni wa Mpulumutsi wace amatuta mizimu. Iye amene a ayenda-yenda nalira. Ponyamula mbeu yakufesa; Adzabweranso ndithu ndi kufuula mokondwera, alikunyamula mitolo yace." (Masalmo 126:6) Ngati ticita ufulu tidzatuta ufulu. Mulungu amalonjeza kwa amene amapereka kuti sadzasowa kanthu kosawasowa. "Iye wakufesa mouma manja, mouma manjanso adzatuta. Ndipo iye wakufesa moolowa manja, moolowa manjanso adzatuta. Ndipo Mulungu akhoza kucurukitsira cisomo kwa inu; kuti inu, pokhala naco cikwaniro conse m'zinthu zonse, nthawi zonse, mukacurukire ku nchito yonse yabwino" (2 Akorinto 9:6,8).

## GAWO 7: IYE ADZAKHALA NAFE PAMENE TIKUCITIRA UMBONI

Werengani Mateyu 28:19-20. Yesu analamulira omutsatira ace kupita kuli konse ndikukapanga ophunzira. Lamulo limeneli ndi lakwa okhulupirira aliyense. Pamene tilimva, mwina timaganiza kuti. "Kodi ine ndikhoza kucita bwanji zimenezi? Ine ndine m'zimai m'modzi, wocepa." Koma Yesu amapanga malonjezo. Iye amalonjeza kuti adzakhala ndi ife nthawi zonse. Motero pamene ticitira umboni, tiyenera kutsimikiza kuti ali pomwepo. Werengani Mateyu 28:18. Yesu ali ndi mphamvu ndi ulamuliro onse. Ngati iye ali ndi ife, palibe cinthu cingatigonjetse. Tikhoza kunena monga Paulo nanenera, "Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo."

mango. Cipatso ca moyo wa Mkristu ndico Akristu ambiri. Mtengo wa zipatso uli onse uyenera kubala zipatso. Mkristu aliyense ayenera kubala zipatso. Tinalonjezedwa zipatso ngati ife "tikhalabe" mwa iye. Anthu amene akhala mwa iye amakhulupirira mwa iye tsiku ndi tsiku la moyo wao. Iwo amapemphera ndipo amayesa kukhala moyo wa cikondi monga wa Yesu. Iwo anauza abwenzi ao za cikondi cace. Yesu amakonda anthu onse. Anthu anamukonda iye; anali kumabwera kwa iye. Magulu a anthu anamutsata iye kuli konse komwe anapita. Munthu amene akhala mwa Yesu amafanana ndi Iye. Iye amakonda anthu cifukwa ndi ofanana ndi Yesu; iwonso amamukonda ndipo amakokedwera kwa Mpulumutsi amene amamutsata m'moyo wace. Anthu amenewa ndi zipatso za moyo wa Mkristu. Tiyeni tifunitsitse kukhala pafupi fupi ndi Yesu Kristu kuti tikhale monga iye ndikuti tikokele kwa iye anthu ambiri.

GAWO 6: TIDZAKOLOLA COMWE TINADZALA

"Musa nyengedwe, Mulungu sanyozeka; pakuti cimene munthu afesa, cimeneco adzacitatu" (Agalatiya 6:7). Miyoyo yathu ndi nchito padziko lapansi pano lidzatuta. Mtundu wa zotuta umadalira zinthu zimene timacita.

Ngati tikukhala miyoyoyo yaucimo, kudzakhala kututa kwa zoipa. Munthu amene amapweteka ena ndi nchito zace zankhanza amatuta cidani. Amakhala opanda abwenzi. Munthu amene amamwa zakumwa zikali, amatuta matenda ndipo mwina mwace umphawi.

Munthu amene amadzala mbeu za cifundo amakhala ndi abwenzi ambiri. "Koma tisaleme



PHUNZIRO 1

MUTU WAPHUNZIRO: BUKU LA YONA

MUTU WALERO: YONA-ATHAWA KWA MULUNGU

NDIME YOLINGALIRA: Macitidwe 10:15,28

MAU APAMTIMA: *"Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimaliziro ca nthawi ya pansi pano."*

*Mateyu 28:19-20*

MTSOGOLERI:

Mwezi uno tiphunzira buku la Yona. Bukuli linalembedwa ndi Yona mneneri wa Mulungu. Dzina lace lakuti Yona limatanthauza kuti nkhunda, zomwe timaziganizira kuti ndi zofatsa, mbalame zacikondi. Mmaphunziro athu, tionamo kuti Yona sanacite zinthu m'moyo mwace nthawi zonse monga ndi tanthauzo la dzina lace.

Yona anali m'neneri ndipo anamva pamene Mulungu anaitana. Mu Buku lace, anaonetsa kuti Mulungu analankhula naye za nchito imene Mulungu anafuna kuti Yona amucitire. Potsiriza iye anaonetsa kuti Mulungu analankhula kwa iye alikubvumbulutsa cifundo ca Mulungu ndi nkhawa yofuna anthu onse adziko lapansi.

## GAWO 1:  KUITANIDWA KWA YONA NDI KUSAMVERA

Mulungu analankhula kwa Yona mu Mutu oyamba, ndime 1-3. Iye anauza Yona kuti apite ku m'zinda waukuru wa Ninive ndikukalankhula zotsutsana ndi macimo ao. Yona anadziwa za Mzinda wa Ninive cifukwa iye anali kukhala pa mseu omwe mitundu ya anthu anali kudzera ndipo anamva za nthano zomwe Mzinda wa Ninive unali kucita. Yona anadziwa kuti unali waukuru ndikuti zoipa zamitundu ili yonse inali kucitika kumeneko.

Yona sanakonde.anthu aku Ninive. Iye sanafune kupita ku Mzinda umenewo ndikukalankhula motsutsana ndi zoipa zimene anali kucita cifukwa iye sanafune kuti alape ndi kupulumutsidwa. Yona anaganiza zothawa kuitana kwa Mulungu. Iye anapita ku Yopa ndikukalipira ndalama zaulendo wa pa sitima popita njira yosiyana ndi ku Ninive.

Popeza anthu aku Ninive anali wocimwa kwambiri, Yona sanaganize kuti anthuwo anafunikira mwai wakuti akhale opulumutsidwa. Iwo anayenera kulangidwa cifukwa ca macimo ao. Yona sanali kuona macimo monga momwe Mulungu amawaonera. Kwa Yona munthu amene anali ndi cimo laling'ono anaganiza kuti anayenera kupatsidwa mwai wolapa, koma munthu yemwe anali ndi macimo ambiri sanayenera kupatsidwa mpata.

Kodi ifenso, monga Yona nthawi zina timaiwala kuti macimo onse, ngakhale kuti ndi okula motani, ndi oipa pamaso pa Mulungu? Kodi kusamvera Mulungu ndi cimo? Mu Luka



dongosolo liri lonse la pa moyo wao koma atayamba apemphera kwa Mulungu kuti awaonetse cifuniro cace. Cifukwa ca ici ciri conse cimene iwo acita cimakhala mucifuniro cace. Adzapereka kwa anthu amenewa mphamvu ya pa mayesero ao. Iwo adzakhoza kucita ciri conse osatopa.

## GAWO 5:  MPHAMVU YACE IMAGONJETSA KUFOOKA KWATHU

Werengani 2 Akorinto 12:9. Paulo anali obvutika cifukwa ca kufooka komwe anali nako m'thupi lace. Iye samachula kufooka; iye anakuca "minga m'thupi." Iye anapemphera kuti Mulungu aicotse, koma Mulungu sanaicotse. Ndipo Paulo anaphunzira kufooka komwe anali nako m'thupi lace kunamukakamiza kuti akhulupirire Mulungu. M'malo mwa kufooka kwace anali ndi mphamvu ya Mulungu. Cisomo ca Mulungu ndi cokwanira tonsefe. Ngati tiri ofooka, tiyenera kukhulupirira Mulungu. Timakhulupirira Iye kwambiri, timapatsidwanso mphamvu zambiri. Tikhoza kusintha kufooka kwathu ndi mphamvu yace. Anthu ambiri amene ali a mphamvu mu matupi ao ndi nzeru zao sakhulupirira mwa Mulungu. Iwo amaganiza kuti ali ndi mphamvu zocita ciri conse mwa iwo okha. Pamene akudzikhulupirira mwa iwo okha ndipo osayang'ana kwa Mulungu, amatsimikiza kuti amalephera. Tiyeni tikhulupirire Mulungu kotheratu ndipo tisinthe kufooka kwathu ndi mphamvu yace.

## GAWO 5:  AMATILONJEZA ZIPATSO

Werengani Yohane 15:5. Ngati tikhala mwa Iye, amatilonjeza zipatso. Cipatso ca mtengo wa olanje ndi olanje. Cipatso ca mango ndi

alikufunsa amai zoyenera kucita, amai ayenera kupempha Mulungu kuti awapatse nzeru asanapereke yankho. Nzeru zace zidzatithandiza ife kumvetsetsa mabvuto a anthu ena motero kuti tikhoze kuthandiza. Koma tiyenera kupempha nzeru zace mwina sizingathe kuperekedwa kwaife.

## GAWO 2: MZIMU WOYERA ADZAKUPHUNZITSANI

Werengani Yohane 14:26. Yesu analonjeza kuti Mzimu Woyera adzatiphunzitsa ndi kutithandiza kukumbukira zonse zimene Yesu adanena. Ngati tifuna kuphunzira, tiyenera kuwerenga Buku Lopatulika. Mzimu wace adzatiphunzitsa ife tanthauzo la mbari imene sitimvetsetsa. Iye adzatithandiza ife kuti timvetsetse ngati sitingathe kuwerenga bwino. Iye adzathandizanso munthu amene sadziwa kuwerenga. Adzathandiza munthu ameneyu kumvetsetsa pamene mau a Mulungu ali kuwerengedwa ndi munthu wina. Iye adzamuthandiza kukumbukira zinthu. Pali Akristu ambiri amene ali ndi maphunziro ocepa, koma amadziwa ziphunzitso za Buku Lopatulika. Mzimu wa Mulungu unawathandiza kuti amvetsetse. Tiyenera kuyesa kuphunzira ndikukhala ndi cikhulupiriro cakuti adzatithandiza. Limeneli ndi lonjezano lace, ndipo malonjezano ace ndi woonadi.

## GAWO 3: ADZAKUPATSANI MPHAMVU

Werengani Yesaya 40:31. Mulungu amalonjeza ana ace kuti adzakhala ndi mphamvu pameyesero. Lonjezano limeneli ndi lakwa amene "ali kudikira pa Ambuye." Kodi ndi anthu ati "amene amadikira pa Ambuye?" Ndi amene nthawi zonse amatsata utsogoleri wace. Iwo amayamba poyamba kufunsa cifuniro cace. Samacita



19:10, Yesu anati, "Pakuti mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa cotaikaco." Aliyense ayenera kukhala ndi mwai wokumva Uthenga wa Bwino kuti apulumutsidwe.

## GAWO 2: YONA PANYANJA

Sitima ya m'madzi imene Yona anakwera inali kupita kutali ndi Ninive. Ulendo utangoyambika, mphepo yolimba kwambiri inafika pa nyanjayo. Mkuru woyang'anira sitimayo ndi gulu la nchito ace anali kupemphera kwa milungu yao kuti iwapulumutse ndi kupulumutsa sitimayo. Yona anali cipinda ca pansi atagona. Kusamvera kwace kwa Mulungu kunamutopetsa kwambiri. Mkuru woyang'anira chomboco anamudzudzula cifukwa cogona tulo kuti sanali kupemphera kwa Mulungu wace.

Pamene ife tikhala osamvera Mulungu, mu mitima yathu mumakhala umbuli wa uzimu. Timayesa kupewa kucita zimene Mulungu afuna kuti ticite, ndipo timatseka malingiliro athu ku zinthu za uzimu. Timadzigonjetsa tokha kuti sizifunikira aliyense. Koma monga kulakwa kwa Yona kunakhudza anthu ogwira nchito mu combo, moteronso ife timakudza anthu amene amakhala moyandikana nafe posamvera kwathu. Pamene mwamuna ndi mkazi akozekera kuti sakhaliranso pamodzi, malingaliro ao amakhudzanso ana, makolo ndi mabanja a akuru.

Paulo amatikumbutsa mu Aroma 14:21, "Kuli kwabwino kusadya nyama, kapena ciriconse cakukhumudwitsa mbale wako." Pamene iwe ukhala osamvera, kodi umapangitsa ena kuti akhumudwe? Pamene uganizira kuti siupita ku mapemphero ndikupita ku msika kapena ku phwando lomwe

liri pa mudzi wina kapena kumzinda, kodi muli kupanga kuti wina wa pa banja lanu kapena wacinansi kuti akhumudwe? Timakonza malingaliro athu tsiku ndi tsiku, tiyenera kuganiza kuti lingaliro liri lonse likhudza motani anthu amene ali motizungulira.

GAWO 3: KULANGIDWA KWA YONA NDI KUSAMVERA KWACE.

Kuyambira pa ndime 8 anthu a pa chombowo anayamba kufunsa Yona mafunso osiyana siyana. Mucikhulupiriro cao ca cikunja, anakhulupirira kuti khalidwe limodzi lomwe munthu anacita mokhudza ena limafunikitsa pa cilango, ngakhale kuti iwo anali osalakwa. Anthu amuchombomo anafuna kudziwa kuti iye anali ndani, anali kucokera kuti, ndikuti anacita ciani kuti coipaco ciwafikire pa anthu onsewo. Kodi inu muli kukumbukira kuti munacita kanthu komwe kanabvutitsa munthu wina? Munthu ameneyo anafuna kudziwa cifukwa cimene munacitira zomwe munacita? Munthuyo amafuna kudziwa cifukwa cimene munacitira osayamba mwafunsa poyamba.

Yona anabvomereza cimo lace. Ngakhale pamene anali kubvomereza cimolo, anakhoza kucitira umboni kwa anthu omwe anali m'chombo. Yona andziwa kuitana kwa Mulungu, iye adayenera kuponyedwa m'nyanja monga cilango cakusamvera kwace. Mulungu sanapange kuti Yona akhale ndi nthawi yofewa pobwerera kwa Iye. Komanso cinali capafupi koposa kuti anthu apachombo onsewo afe.



PHUNZIRO 11

MUTU WAPHUNZIRO: MALONJEZO AMULUNGU

MUTU WALERO: MALONJEZO ONENA ZA NZERU MPHAMVU NDI UTUMIKI

MAU AMULUNGU: Afilipi 4:8-20

MAU APAMTIMA: *"Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo."*
*Afilipi 4:13*

MTSOGOLERI:

Akristu ena amaona kuti sangacite zinthu zina zomwe Mulungu amafuna omutsatira ace kumacita. Ena amati, "Ndine osaphunzira. Sindidziwa macitidwe ace." Ena amanena kuti "ndilibe mphamvu yocitira." Ndipo ena amati sindingathe. Nditsimikiza kuti ndilephera." Mulungu amatipatsa malonjezo ena otithandiza mu moyo wathu wa Cikristu ndi pocitira umboni. Tiyeni tione pa malonjezo ace a za nzeru. Mphamvu ndi utumiki.

GAWO 1: ADZAPEREKA NZERU

Werengani Yakobo 1:5. Mulungu amalonjeza kutipatsa nzeru pamene tizipemphera. Nzeru zace zidzatithandiza kusankha njira yoonadi. Nthawi zambiri cimakhala cobvuta kudziwa njira yabwino. Nthawi zina njira ziwiri zimaoneka ngati njira zabwino. Amalonjeza kutithandiza kusankha njira imodzi imene ili njira yace. Nzeru zace zidzathandiza azimai pamene alikuphunzitsa ndi kuweruza ana ao. Pamene mwana

Tiri ndi lonjezo kuti Mulungu adzakhululukira ngati tilapa macimo athu. "Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera colungama ciri conse" (1 Yohane 1:9). Iye amalonjeza "Ndipo akacimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Yesu Kristu wolungama" (1 Yohane 2:1).

KUTSIRIZA:

Sitiyenera kumadandaula. Mulungu analonjeza kuti adzatipatsa zosowa zathu. Iye adzatinsenzera nkhawa zathu. Adzatipatsa wotitonthoza Mzimu Woyera, kutithandiza mu nthawi ya mabvuto. Iye adzatipatsa cimwemwe pamene tiri kubvutika cifukwa ca dzina lace. Sadzalora kuti ife tibvutika kuposa mphamvu zathu. Ngati ticimwa, adzatikhululukira. Tiyeni tidalire pa iye motheratu.

PEMPHERO:



Anthu amene anali pa chombopo poyamba anayesa kuti abwerere pa gombe la nyanja. Ndipo posacedwa anazindikira kuti anayenera kungoponya Yona m'nyanja. Mulungu anakonza cinsomba ca cikuru kuti cimeze Yona. Monga Yona anali m'mimba mwa nsomba masiku atatu ndi usiku utatu ndipo kunabwera cipulumutso, moterenso Yesu Kristu anali mkati mwa dziko atakwiliridwa kwa masiku atatu ndi usiku wace ndipo anauka kutipatsa cipulumutso kupyolera mwa Kristu wa moyo. (Mateyu 12:39-40).

MTSOGOLERI:

Muphunziro lathu la lero taona zomwe zimacitika pamene munthu samvera Mulungu. Yona anadana ndi anthu aku Ninive ndipo sanafune kuti iwo apulumutsidwe. Komatu imeneyi sinjira ya Mulungu, njira ya cidani. Mulungu amakonda anthu amitundu yonse. Iye anafuna kupatsa anthu ku Ninive mwai wolapa. Mulungu anakondabe Yona ngakhale pamene iye sanamvere. Iye analanga Yona, koma anathandiza Yona kuti abwerere kumalo omwe anayenera kucita zozidwa.

Yona anapulumutsidwa cifukwa ena olingalilapo pamene muli kupemphera. Kodi Akristu nthawi zina amadana ndi anthu cifukwa ocokera ku ku mtundu wina? Kapena kuti apanga ndalama zambiri? Kapena kuti ndi ophunzira kwambiri? Kodi imeneyi ndi njira ya Mulungu?

PHUNZIRO 2

MUTU WAPHUNZIRO: BUKU LA YONA

MUTU WALERO: YONA-ATHAMANGA NDI MULUNGU

NDIME YOLINGALIRA: Ahebri 12:1,5-6

MAU APAMTIMA: *"Titaye colemetsa ciri conse, ndi cimoli limangotizinga, ndipo tithamange mwacipiriro makaniwo adatiikira."*
*Ahebri 12:1b*

MTSOGOLERI:

Lero tipitiriza kuphunzira za Yona pamene anatembenuka kwa Mulungu. Mulungu analanga Yona cifukwa anamukonda. Pamene Mulungu akutilanga, sitiyenera kukhumudwitsidwa. Mulungu amalanga ana ace cifukwa Iye amawakonda. Iye amafuna kumvera kwathu ndipo pamene tisocera, iye amatikumbutsa kuti alikutiona potilanga.

Panthawi imene tiri kulangidwa ndi cinthu cikhoza kutukuka mwa izi. Cimakhala cinthu cowawa kwambiri panthawi imeneyo. Mu Ahebri 12:11b Paulo amatiuza kuti, "koma citatha, cipereka cipatso ca mtendere kwa iwo ozolowe-retsedwa naco, ndico ca cilungamo."

GAWO 1: PEMPHERO LA YONA CIOMBOLO

Kodi mukhoza kuganizira wina kuti akhoza kukhala okondwa m'mimba mwa cisomba cacikuru? Yona anali otero. Iye anakondwa cifukwa anapulumutsidwa kuti asamile. Analangidwa cilango ca imfa la thupi. Cotsatira cinali



tsa mabvuto amene ali patsogolo pathu. Amene akonda Mulungu ndikukhala pafupi naye adzapeza njira yopirira mayesero kapena kuwazemba. Munthu amene amakhulupiriradi Mulungu sangane-ne kuti, "Sindikadacita, koma mayesero anaku-la." Mulungu sadzalora kuti tiyesedwe kuposa luntha lathu. Ngati tidzipereka kumayesero, ndi cifukwa cakuti tisowa cikhulupiriro.

GAWO 6: ADZAKHULULUKIRA

Davide anacita cimo lalikuru. Anagwiri-tsa mphamvu zace monga mfumu kutumiza munthu ku nkhondo akaphedwe cifukwa iye anafuna mkazi wace. Iye anali ocimwa cifukwa ca cilakolako ndi kupha. Anawilingura mkati mwa mtima wace cifukwa ca cimo limene anapanga. Anadzigonjetsa yekha kuti monga mfumu akada-khoza kutenga yemwe anafuna anamufuna. Ngakhale kunali tero Davide anakonda Ambuye. Pamene Natani m'neneri adaonetsa Davide cimo lace, anadzioneratu kulakwa kwace. Iye anasi-ya kuwilingura cifukwa ca kulakwa kwace. Ana-tembenukira kwa Mulungu nabvomereza cimo lace, kupempha cikhululukiro. Mulungu anamukhululu-kira ndipo Davide anapitiriza kutumikira Mulungu. Mukhoza kuwerenga Masalmo 51 pemphe-ro lolapa la Davide.

Nthawi zambiri ndi cinthu cobvuta Akristu kuona zolakwa zomwe acita. Ndipo nthawi zina pamene tiona macimo athu sitimafuna kuwazindi-kira. Akristu ena amene ali ocimwa amabvutika cifukwa ca zolakwa zao zomwe amayesa kuzibisila Mulungu. Cifukwa ca macimo ao amaleka kupita ku chalichi kapena kugwirizana ndi Akristu ena. Iwo samabvomereza macimo ao monga Davide anacitira.

anauza kuti alikupita kwa Atate, koma MTHANDIZI adzabwera mmalo mwace kudzakhala nao. Ameneyu ndi Mzimu Woyera. Iye alipo wokonzeka kuthandiza ife pamene tibvutika cifukwa ca cikhulupiriro ca mwa Yesu Kristu akhoza kukhala wokondwa cifukwa akudziwa kuti Yesu mwini wace alondedwa. Ngakhale kuti moyo wace wa pa dziko lapansi ukhale obvutika, Mkristu analonjezedwa mphotho m'mwamba. Ngati munthu abvutika cifukwa anacita zolakwa amayenera cilango cimene akucilandiraco. Iye alibe cifukwa comwe angakhalire okondwa m'mabvuto ace. Akristu amabvutika mnjira zosiyana siyana cifukwa ca cikhulupiriro cao. Ena amamenyedwa ndi kuikidwa mukaidi. Ena amacotsedwa ndikupitikitsidwa ndi apa banja ao. Koma Akristu ambiri samabvutika m'njira zimenezi. Ayenera kuima molimba mu cikhulupiriro cao ngakhale kuti ena ali kuwaseka kapena kuwanyogodola. Iwo ayenera kukhala okhulupirika kwa Yesu Kristu ngakhale kuti mabanja ao onse ndi abwezi ao atsata njira zaucidakwa kapena za matsenga. Mwina akhoza kunyozedwa ndi kunyozedwa cifukwa cokana kutenga mbari ya m'njira yofanana ndi zocita zao, Mkristu amabvutika mu njira zimenezinso, ndipo malonjezo a Mulungu ali kwa amene amakondwera mumasautso cifukwa ca cilungamo.

GAWO 5: ADZAKUTHANDIZANI M'MAYESERO

Werengani 1 Akorinto 10:13. Mayesero amene tiri nao ndi amtundu amene amabwera kwa anthu. Sitidzakhala ndi mayesero amene ali akuru kupirirako. Limeneli ndi lonjezano locokera kwa Mulungu. Iye sadzalora kuti ife tiyesedwe kuposa mphamvu zathu. Iye adzatipatsa mphamvu yonyamulira mabvutowo. Adzatione-



kukonzanso kwa moyo wa uzimu. Yona anazindira kuti Mulungu ndiye anali kulamulila. Anaona coipa ca kusankha njila yace m'malo mwa njira ya Mulungu pamene anaphunzira phunziro limeneli, anakozekera kucita cifuniro ca Mulungu.

Yona sanangokhala masiku atatu ndi usiku wace m'mimba mwa nsomba monga Kristu anakhalira m'manda. Iye, monga Kristu, anapereka moyo wace cifukwa ca anthu adziko. Anthu amene anali pa chombo (akunja) anayerekezedwa anthu a dziko lapansi. Yona ndiye anali mu Yuda yekha mu chombomo. Iye anawapulumutsa pobvomereza kuti amuponye mnyanja.

Mai wina amene anali kukhala pafupi ndi ine nthawi ina anapsa kwambiri. Anthu anaopa kumuyang'ana, ngakhale mwana wace wamwamuna. Poyankha funso langa pa zomwe zinaoneka, munthu wina okhala pafupi naye ananena nthano. Pamene mwana wamwamunayo anali wamung'ono, nyumba yao idayaka ndi moto. Mai wa citsikanayo, adangofika kucokera kotunga madzi, nathamangira m'nyumba kuti akapulumutse mwana wace amene anagona tulo. Maiyo anateteza mwanayo ndi thupi lace. Ndipo cotsatira cace anali pafupi kufa cifukwa ca mabala opsa ndi moto. Anthu okhala pafupi ndi iwo anati anada nkhawa cifukwa mwana wamwamunayo anali kuseka mai wace ndipo anali wosamvera. Ena anafunsa monga ngati moyo wace uli oyenera momwe anapyulamo. Yankho locokera kwa mai ace nthawi zonse linali kubwera mwamsanga, "Ndikhoza kucitanso kuti ndipulumutse mwana wanga."

Kodi ndi angati aife tingadzipereke kufera ena? Mwina cikhoza kukhala capafupi

kudzipereka tokha cifukwa ca mabanja athu okha koposa mitundu ina kapena dziko lathu. Koma Mulungu alikutionetsa ife kupyolera mu nthano ya Yona ndi Kristu kuti tiyenera kupita kwa anthu onse adziko lapansi osangoti okhao amudzi kapena Mzinda wathu okha.

GAWO 2: KUMVERA KWA YONA

Mu Yona 3:1 Mulungu anauzanso Yona kuti apite ku Ninive kukalalikira Uthenga umene Mulungu anamupatsa iye. Yona anamvera Ambuye ndipo anapita ku Mzinda waukuru wa Ninive. Mzindawo unali waukuru kwambiri kotero unatenga masiku atatu kuyenda mouzungulira. Atangoyenda tsiku limodzi mu mzinda waukuruwo Yona anayamba kucenjeza anthu kuti kwatsala masiku makumi anai kuti mzindawo uonongeke. Iye ananyamula uthenga wa Mulungu ndi kupereka kwa anthu aku Ninive.

Taganizirani za malo amene angakutengereni masiku atatu mulikuyenda kuti mukafike. Tsopano ganizirani kuti malo onsewo ndi odzala ndi anthu nyumba zace ndizomangidwa pafupi. Mnjira imeneyi, mukhoza kukhala ndi lingaliro la kakulidwe komwe Ninive analiri. Popeza Yona anamvera, anapatsa mwai anthu amene anadzala mzindawo kuti alape. Kodi ife tiri kumvera ndi kupindula anthu otaika kuti alandire Yesu monga Mpulumutsi wao? Kodi inu munakana kupita ndikukawauza cifukwa cakuti ocimwa onsewo afunika kufa? Kodi inu nthawi zina mukhoza kuchedwa Yona? Pamene wina wace salikumvera Mulungu, ambiri akhoza kufa cifukwa cakusamverako.



za mafumu. Yesu anati tizifuna zinthu za uzimu poyamba ndipo Mulungu adzatipatsa zosowa zathu. Iye samanena kuti tikhale aulesi ndikuyembekezera Mulungu kutipatsa cakudya ndi zobvala ngakhale tikugwira nchito. Iye anafuna kuti tikhale ndi cikhulupiriro mwa iye osati kungotaya nthawi yathu kudandaula za ndalama ndi zinthu. Anthu ambiri samakhala okondwa. Iwo amakhala nthawi yao yonse ndi mphamvu yao kudandaula za kupeza zakudya ndi zobvala za tsiku lina. Tiyeni tithokoze Mulungu tsiku ndi tsiku cifukwa ca zinthu zomwe tiri nazo. Tiyeni tigwire nchito molimbika; ndipo khulupiriráni iye kuti zinthu za mawa adzacita.

GAWO 2: ADZATITENGERA ZOBVUTA ZATHU

Werengani Mateyu 11:28-30. Akristu ena ali ndi mabvuto olemera kwambiri powanyamula. Mkazi amene mwamuna wace wamwalira ali ndi udindo wakukuza ana ace. Akazi ena ali ndi amuna amene amawamenya. Akazi ena amayenera kugwira nchito molimba ngakhale moyo wao siuli bwino. Anthu ena amaopa imfa. Zimenezi ndi akatundu olemera kuwanyamula. Yesu adziitanira aliyense amene atenga akatundu olemera. Iye amalonjeza kuwapatsa mpumulo. Iye akuti kutenga mtanda wace. Ndi wopepuka ndi wosabvuta kunyamula. Mu 1 Petro 5:7 tiwerenganso lonjezo limeneli kaciwiri, "ndi kutaya pa Iye nkhawa yanu yonse, pakuti Iye asamalira inu."

GAWO 3: IYE ADZAPEREKA MTHANDIZI

Werengani Yohane 14:16. Yesu analonjeza kuti sadzasiya omutsatira kukhala okha. Iwo anali kudandaula ndi kucita mantha. Iye

PHUNZIRO 10

MUTU WAPHUNZIRO: MALONJEZO A MULUNGU

MUTU WALERO: MALONJEZO ONENA ZA MADANDAULO NDI MAYESERO

MAU AMULUNGU: Masalmo 23

MAU APAMTIMA: *"Ndi kutaya pa iye nkhawa yanu yonse, pakuti Iye asamalira inu."*

*1 Petro 5:7*

MTSOGOLERI:

Akristu ambiri amaciona kuti ndi cinthu cobvuta kwambiri pamene ali ndi bvuto loyamba. Cimakhala cobvuta koposa pamene ali ndi abale omwe si Akristu akuwatsutsa zonse zomwe acita. Davide analinso ndi bvuto lotere. Iye anati, "Pakuti ndinacita nsanje odzitamandira, pakuona mtendere wa oipa." Masalmo 73:3 Mulungu anapereka malonjezo ambiri kwa ana ace a za madandaulo ndi mabvuto amene ali nao pano pa dziko lapansi. Tiyeni tione ena a mabvuto lero.

GAWO 1: ADZATIPATSA ZOSOWA ZATHU

Werengani Mateyu 6:33. Kodi munayamba mwadera nkhawa cakudya ca pa banja lanu? Kodi muyamba mwadandaula cifukwa mulibe zobvala zabwino? Yesu amatiphunzitsa kuti Mulungu amapereka zosowa zathu zonse. Atate wakumwamba amadyetsa mbalame. Kodi inu sindinu oposa zimenezi? Kodi bwanji kudandaula cifukwa ca zobvala? Mulungu amapanga maluwa ndipo amakhala okongola kuposa zobvala



GAWO 3: NINIVE ALAPA

Anthu aku Ninive anakhulupirira ndipo analapa. Iwo anasala cakudya ndikubvala ziguduli. Ziguduli zinali ubweya wa mbuzi umene anali kubvala mthupi pa nthawi ya kulila. Pamene mfumu inamva, inatumiza lamulo kwa onse kuti munthu aliyense kapena ciweto cisadye kapena kumwa ndipo munthu aliyense kubvala ciguduli. M'malapidwe oterewa ndikudzikhutula, mwina mwace Mulungu akhoza kupulumutsa mzindawo. Iwo anaika ciyembekezo cao pa kusala kuti Mulungu anatumiza cenjezo. Iwo anali otsimikizadi kulapa kwao. Mulungu anaona nchito zao ndikuti analapadi. Mulungu anapulumutsa Ninive.

Yona anafunsidwa kuti acenjeze anthu aku Ninive. Cocita cina cinali ca kwa anthuwo eni ace. Iwo akanasankha kusalapa. Cisankho cinali cao, ndipo Mulungu anabvomereza kulapa kwao. Udindo wathu ndi wocitira umboni. Mzimu Woyera umapulumutsa mizimu. Mulungu mwina sangatitumize ku Mzinda njira yomwe anacitira Yona, koma iye amatitumiza kwa anthu amene timakumana nao tsiku ndi tsiku. Ngati titapita ku Banki, ku msika, ku positi ofesi, kukacezera anansi, timakhala ndi mwai ocitira umboni kwa wina wace za Yesu. Ngati tiri kuthamanga ndi Mulungu, tidzayesa tsiku ndi tsiku kuti wina wace adziwe uthenga wabwino wa cipulumutso ca mwa Yesu Kristu.

MTSOGOLERI:

Ndicinthu cokondweretsa kuona anthu ali kupinduludwa kucokera kucionongeko cao. Iwo analapa mwamsanga, ndipo Mulungu anawaombola.

Cimakhala cimwemwe cacikuru kwa ife pamene ticitira umboni kwa anthu otaika ndikuwaona kuti alapa ndi kubvomereza Yesu Kristu monga Mbuye ndi Mpulumutsi.

Pamene tiri ndi nthawi yamapemphero, tiyeni tilembe maina a anthu ana ndi malo amene tiri kuwadziwa omwe asoweka kumva za ciono-ngeko cao. Tiyeni tikambirane panthawi yoce-pa za momwe angapindulidwire. Ngati iwo ali pafupi nafe, kodi tingakhonze m'mene tingawa-citile umboni? Ngati ali kutali kodi kumene-ko kuli wacimishoni amene tingamupempherere, kapena tiyenera kupempherera amene angatumi-dweko?

Tsopano tiyeni titenge nthawi yopemphere-ra mwai ocitira umboni wa za Yesu kwa ena. Potsiriza, pempherani kuti mukhale mboni za Yesu zolimba.



ni Aroma 8:26,27.

KUBWEREZA: Kodi mukhoza kufotokoza tanthauzo la mau a Mulungu otsatirawa?

1. Muyenera kupempha. Mateyu 7:7

2. Khalani mwa Iye. Yohane 15:7

3. Pempherani ndi cikhulupiriro. Mateyu 21:22

4. Khululukirani ndipo funani cikhululukiro. Marko 11:25,26

5. Pempherani mtseri. Mateyu 6:6

6. Pempherani ndi anthu ena. Mateyu 18:20

7. Mzimu Woyera adzathandiza. Aroma 8:26,27

PEMPHERO:

Cikhululukiro cimacotsa zokhumudwitsa njira, tiyenera kupempha Mulungu kuti atikhululukire macimo athu. Macimo athu akhoza kuima pakati pa ife ndi Mulungu. Tiyeni tizikhululukire ena cifukwa ca zinthu aticitira ife. Tiyeni tizipempha ena kuti atikhululukire ngati tacita cimo kwa iwo. Tiyeni tipemphe Mulungu kuti atikhululukire.

## GAWO 6: KUPEMPHERA MODZIKHUTHULA

Werengani Mateyu 6:6. Pamene Yesu anali padziko lapansi pano panali anthu amene anafuna kuti ena awaganizire kuti anali abwino ngakhale kuti sanali otero. Motero iwo anali kumaina m'malo amene anthu ambiri akadamaona ndikumapemphera ndi mau okweza. Yesu anati anthu amene anali kucita zinthu zotero analandiriratu mphotho yao. Iwo anafuna kuti anthu awaone ndikuwayamikira. Iye anauza omutsatira ace kuti asacite zotere. Ngati muli kufunadi KUPEMPHERA KWA Mulungu cilibe kanthu kuti wina wakuona kapena ai. Iye anati muyenera kupita kumalo apadera a chete mungamapemphere mwacinsinsi. Ndipo Mulungu adzamva ndipo iye adayankha. Mulungu analonjezanso kuti pamene alikupemphera ngakhale mwina atangokhala anthu ocepa. Werengani Mateyu 18:20.

## GAWO 7: MZIMU WOYERA ADZATHANDIZA

Nthawi zina mkazi amafuna kupemphera kwa Mulungu, koma mwina sadziwa zoyenera kunena. Mtima wace ndi olemera motero kuti sakhoza kupeza mau akuti afotokozere Mulungu zosowa zace. Mulungu analonjeza ife thandizo la Mzimu Woyera pamene sitidziwa mapempheredwe. Werenga-



# PHUNZIRO 3

MUTU WAPHUNZIRO: BUKU LA YONA

MUTU WALERO: YONA-ATHAMANGA PATSOGOLO PA MULUNGU

NDIME YOLINGALIRA: Hoseya 12:6

MAU APAMTIMA: *"Khalani cete, ndipo dziwani kuti Ine ndine Mulungu."*
*Masalmo 46:10*

MTSOGOLERI:

Lero titsiriza kuphunzira Buku la Yona. Poyamba Yona anafuna kuthawira Mulungu ndi lamulo lace. Posacedwa anapeza kuti sungathawire Mulungu ndi kumubisalalira. Mulungu ali kuli konse. Atangotha kulapa, Mulungu anapatsanso Yona nchito yace. Potsiliza anayamba kuyenda ndi Mulungu. Koma lero tipeza mu ndime yacinai kuti Yona ali kuthamanga patsogolo pa Mulungu. Nthawi zambiri timadzipeza tokha, tiri monga Yona, tikuyesa kuthamanga ndi Mulungu, koma tiri kuthamanga patsogolo pa Mulungu.

Mu Buku la Hosea timakumbutsidwa kuti tiyenera kudikira pa Ambuye. Mu Hoseya 12:6 timapeza kuti, momwemo utembenukire kwa Mulungu wako, sunga cifundo ndi ciweruzo, nuyembekezere Mulungu wako kosalekeza." Simuyenera kukhala patsogolo pa Iye, koma kudikira Mulungu. Thamangani ndi Mulungu.

Ambiri aife tiri ndi anthu apa banja lathu, abwenzi, kapena amene tikhala nao pafupi, amene tiyenera kuona kuti abvomereza Yesu

Kristu monga Mpulumutsi wao. Nchito ikhoza kukhala yapafupi ngati ife tikadabvomera kuti tiwauze. Kapena tikadawakakamiza kuti abwere kwa Yesu. Komatu imeneyi sinjira ya Mulungu. Munthu aliyense ayenera kupanga cisankho cace. Nthawi zina timafuna kucita zinthu nthawi isanakwane. Timathamanga mtsogolo mwa dongosolo lo la Mulungu m'malo molankhula ndi iye ndi kuyenda ndi Iye. Timakhala ndi mabvuto monga Yona.

GAWO 1: KUSAKONDWA KWA YONA

Mai ine, Yona anali wosakondwa. Ukali wace unali wotentha kuyambira pa mutu kufikira m'mapazi ace. Kunyada kwace kunapwetekeka cifukwa anapangidwa kuti aoneke ngati mneneri wonama. Iye sanadere nkhawa za ulemu wa Mulungu. Iye anadera nkhawa ulemu wace okha. Iye analankhula kwa Mulungu za nkhaniyo. Iye anati, tsopano Ambuye, cimeneci ndico cifukwa cace ndinathawira poyamba paja. Ndinadziwa kuti mudzacitira cifundo anthu oipawa. Tsopano ine mwandipusitsa. Iwo andiseka ine ndikunena kuti ndife." Yona anali wodera nkhawa ulemu wace monga mneneri, kuti iye anasowa cisangalalo ca anthu pakuti analapa.

Pamakhala nthawi zina zomwe timalephela kucitira umboni kwa munthu m'modzi cifukwa timacita mantha kuti atiseka. Tidziwa kuti ayenera kumva, koma sitifuna kunyozedwa. Mwina tikhoza kukaika-kaika kufuna kugwiritsa nchito cilankhulo ca anthu ena kapena mtundu mwina akhoza kutiseka machulidwe athu. Tiyenera kukumbukira kuti Yesu ananyozedwa. Anamuseka ndi kumumenya Iye. Koma lilemekezeke dzina lace, Yesu anafa naukanso kuti tikhale ndi moyo wosatha.



Mulungu. Ngati mau ace akhala mwa ife, tidzapempherera zinthu zimene zogwirizana ndi mau ace. Motero Mulungu ndi okozekera kuti patsa ife ciri conse cimene tingapemphe. M'malo ena a m'Buku Lopatulika timauzidwa kupemphera "Mdzina lace" ndipo tidzapatsidwa cinthu cimeneci sicikutanthauza kuti tidzinena mau amenewa mupemphero liri lonse. Cikutanthaudza kuti tiyenera kupemphera zinthu zokha zimene mu cifuniro ca Mulungu, zinthu zimene Yesu mwini akadakazipempherera.

GAWO 4: KUPEMPHERA MWACIKHULUPIRIRO

M'mawa wina Yesu ndi ophunzira ace anali ndi njala. Iwo anaona mtengo wa mkuyu umene unali ndi masamba okha amene ngakhale kuti inali nyengo yobereka zipatso. Yesu anali, "Kuyambira lero mtengo uwu siudzabalanso cipatso." Pamene analankhula, mtengo unafota. Akuphunzira anadabwa, koma Yesu anawauza kuti asadabwe pa zimenezo. Iye anati cimeneci ndi cinthu cocepa, koma ngati akadakhoza kusuntha mapiri. Iye anati, "Ndipo zinthu ziri zonse mukazifunsa m'kupemphera ndi kukhulupirira mudzadzilandira" (Mateyu 21:22). Mulungu analonjeza kucita zinthu zimene anthu anaganiza kuti ndizosatheka ngati tipemphera mwa cikhulupiriro.

GAWO 5: KUKHULULUKIRA NDIKUFUNA CIKHULULUKIRO

Werengani Marko 11:25,26. Mulungu asanamve mapemphero athu, tiyenera kukhululukira ena. Ngati ife sitikhululukira ena, Mulungu sangatikhululukire. Udani ndi mikangano imatsekereza ciyanjano cathu ndi Mulungu.

## GAWO 2: KHALA MWA IYE

Mu Yohane 15:1-7 Yesu anadziyerekeza yekha ndi mpesa. Ngati nthambi zidulidwa ku mpesa zimafota. Zimakhala zaponda moyo zikhala pa zokha. Sizikhoza kubala zipatso. Sizingapindule kanthu. Akristu ali otere. Ngati acotsedwa kucokera kwa iye, miyoyo yao ndiyopanda nchito. Pamene iwo akucitira umboni, amangolankhula mau opanda nchito. Mau ao alibe mphamvu cifukwa anadulidwa kucokera kumene mphamvu imacokera. Koma pamene nthawi ikhalabe mu mpesa, mphamvu yocokera mu mpesawo imafalikira mu ntambi iliyonse. Nthawi iliyonse imagawana mphamvu ya mpesa. Nthambi iliyonse ikhoza kubala zipatso. Munthu amene amakhala pafupi ndi Yesu Kristu ali wofanana ndi cimeneci. Amakhala ndi moyo wosatha. Iye amalandira mphamvu yace kucokera kwa Yesu. Iye amagawana mu mphamvu yace. Iye akhoza kupempha zomwe akufuna ndipo zidzacitika. Iye akhoza kucitira umboni ndi mphamvu. Adzabala zipatso. Sali kanthu mwa iye yekha. Ngati iye alumikizidwa ndi mpesa, Yesu Kristu, akhoza kucita zinthu zonse. Pemphero limatilumikiza ndi Yesu Kristu.

## GAWO 3: PEMPHANI ZOMWE MUFUNA

Werengani Yohane 15:7. Mulungu amalonjeza kuti ngati tikhalabe mwa iye ndikuti mau ace akhale mwa ife adzatipatsa ciri conse cimene tidzapempha. Kodi tanthauzo lacimeneci ndi ciani? Kodi tikhoza kulandira ciriconse cimene tipempha? Inde, ngati tikhala mwa iye, sitidzapempha zinthu zobweretsa ulemerero kwa ife eni. Sitidzapempha zinthu zomwe zingakhumudwitse umboni wa Cikristu kapena zinthu zimeme zingakhumudwitse nchito ya anthu a



## GAWO 2: YONA NDI MSATSI

Pamene Ambuye anamva Yona akunena kuti kunali kwabwino kufa koposa kukhala ndi moyo Ambuye anafunsa Yona kuti anakwiya cifukwa ciani. Yona anapita kunja kwa mzinda, nadzipangira yekha tsanja, nakhala pansi pa tsanjalo kuti adikire ndikuona zomwe zingacitike. Pamene anali pamenepo kubvutika ndi dzuwa, Mulungu anapanga kuti ka mtengo kamere ndi kukula kuti kaphimbe Yona ndi kumupatsa mnthunzi kuti amve bwino. Yona anakondwera ndi mthunziwo. Iye anali monga mwana wamng'ono amene anaturuka nakhala pansi ndipo anabvutika cifukwa sakanakhoza kupita kunyumba ya bwenzi lace. Ndipo amai ace abwera namupatsa madzi odzidzira. Iye anakondwera kulandira madzi, koma mwangozi madziwa anataika. Ndipo anakwiyanso. Cenjezo linabweranso ndipo anapangitsa kuti kamtengoko kafe. Pamenepo Yona anakwiya nakonzekera kufanso. Mphepo inali yotentha ndipo dzuwa linatentha. Yona anali pafupi kukomoka. Motero anaona kuti kunali kwabwino kwa iye kuti afe.

Yona anali kucita monga mwana ndikungoganiza za iye yekha. Kodi ife tinacita monga Yona nthawi zina? Pamene m'ndandanda sunacitidwe m'njira imene tikufunira kuti ucitikire, kodi timabvutika ndi kukana kucita nao? Mu Buku la Aefeso, Paulo alikutikumbutsa ife kuti sitiyenera kukhala monga ana mu uzimu, koma tiyenera kukula monga Akristu ndi kulemekeza Kristu. (Werengani Aefeso 4:14-16). Sitiyenera kupitiriza kuganiza za ife tokha. Tiyenera kumakula kuti tikhale monga Kristu ndi kumakhala miyoyo yathu tsiku ndi tsiku kuti anthu ena adzadziwa kuti Yesu ndiye

Ambuye a miyoyo yathu.

GAWO 3: YONA APHUNZIRA ZA CIFUNDO CA MULUNGU

Yona 4:9 iwonetsanso Mulungu alikufunsa Yona kuti ndicifukwa ciani akalipa. Mulungu anadzudzula Yona ndikumuonetsa comwe ciyenera kukhala coyamba. Iye anakumbukira Yona kuti anabvutika moyo cifukwa ca kamtengo komwe sanabvutike kuti kamere kapena kukagwirira nchito. Mulungu anati kwa Yona iwe ukalipira ka mtengo komwe kanakula tsiku limodzi ndi kuonongeka patsiku limodzi, koma Mulungu anati ndi cifundo cifukwa ca anthu mazana makumi awiri ndi mphambu makumi awiri (120), ndi ng'ombe zambiri zomwe zinali ku Ninive. Kodi ndi cifukwa ciani Yona anabvutikira kamtengo ndi kuti analibe cifundo kwa anthu a mu mzindamo? Kodi mthunzi wa Yona unali opambana koposa miyoyo ya anthu onse a mu mzinda wa Ninive? Mulungu anali kukumbutsanso kapena kuonetsa Yona kuti Iye amakonda zololedwa zonse.

Osati anthu okha, koma ngakhale ng'ombenso. Ndipo Mulungu anawerenga anthu kapena ana amene sakanakhoza kudzithandiza okha, osapatikiza amene anadziwa dzanja lamanja ndi lamanzere.

Mulungu analenga zinthu zonse ndipo ali ndi cifundo cifukwa ca zinyama monga anacitira pa anthu. Ngati tiri oyenera kukula monga Akristu, tiyenera kukonda zinthu zonse monga momwe Mulungu akondera zinthu zonse. Tiyenera kukhala ndi cifundo ca pa anthu ndikuwacenjeza. Tiyenera kukumbukira ana amene sadziwa kucita cabwino kufikira titawaphunzitsa. Tiyenera



PHUNZIRO 9

MUTU WAPHUNZIRO: MALONJEZO A MULUNGU

MUTU WALERO: MALONJEZO AZA MAPEMPHERO

MAU AMULUNGU: Yohane 15:1-7

MAU APAMTIMA: *"Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'macitidwe ace."*

*Yakobo 5:16b*

MTSOGOLERI:

Lero tikhale tiri kuganizira za malonjezo apemphero. Kupemphera ndiyo njira yathu yolankhulana ndi Mulungu. Ciyambire ca nthawi anthu akhala alikupereka zopempha za kwa Mulungu. Anthu ena amapereka zofunsa zao kwa milungu ya miyala kapena zolengedwa zina. Milungu imeneyi siingamve ndi kuyankha mapemphero ao. Kodi Mulungu anamva mapemphero anu? Kodi Iye adzayankha?

GAWO 1: MUYENERA KUPEMPHA

Mulungu akhoza kumva mapemphero anu ngati mupempha. Ngati simupemphera, malonjezo a za mapemphero sangakhale anu. Yesu anati, "Pemphani ndipo cidzapatsidwa kwa inu, funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu" (Mateyu 7:7). Ngati mwana wanu atakupemphani kuti mumupatse madzi akumwa, mumamupatsa. Ngati iye sapempha, simumupatsa ngakhale madzi alipo. Madziwo ndi ace ngati atapempha. Mulungu amatikonda ife. Ife ndife ana ace ndipo amafuna kutipatsa zinthu zabwino. Iye ndi okonzeka kumva ngati tipempha.

2. Munthu amene akhulupirira akhala ndi moyo wosatha tsopano Yohane 3:36.

3. Munthu amene sakhulupirira sadzakhala ndi moyo wosatha Yohane 3:36.

4. Munthu amene akhulupirira mwa Yesu ndi olengedwa watsopano. 2 Akorinto 5:17

5. Moyo umene Yesu amapereka umakhutiritsa. Yohane 4:14

6. Mulungu adzasunga okhulupirira ku nthawi za nthawi. Yohane 10:28

Kodi munakhulupirira mwa Yesu Kristu? Ngati sikotero, kodi mukhoza kukhulupirira lero? Ngati mwacita, muthokozeni cifukwa ca malonjezo ace odabwitsa.

PEMPHERO:



kusamalira ndi kukonda zinyama zosalankhula. Tiyenera kuphunzira cikondi ca Mulungu.

MTSOGOLERI:

Pali zinthu zambiri zophunzira kucokera m'nthano ya Yona. Pamene tiri kufika kumapeto a bukuli, tinaonatso kuyerekeza ndi Ambuye wathu Yesu. Mulungu aonetsa Yona kuti Iye amakonda anthu onse. Mtundu kapena pfuko kwa iye zilibe kanthu.

Yesu amatilamulira kuti tipite ndi kukawauza za mbiri ya bwino ya cipulumutso. Pamene gulu limodzi labvomereza, tiwaphunzitse ndikuwapanga kuti akhale ophunzira (Mateyu 28:19-20). Pamene iwo akana, tisanse fumbi kumapazi anthu ndikucoka kuti tikapatse gulu ina mwai wakumva uthenga wabwino.

Pamene tiri kutsiliza maphunziro a Yona, tiyeni titenge nthawi yodzipempherera tokha.

1. Kuti tisamaonetsa tsankho pocitira umboni wa Ambuye wathu Yesu.

2. Kuti tikhale nao mwai sabata ndi sabata wotsogolera munthu wina wace kwa Yesu. Zikhoza kukhala kuti tatsogolera athu 52 pa caka.

PHUNZIRO 4

MUTU WAPHUNZIRO: **KODI CINGATISIYANITSE NDI CIANI KU CIKONDI CA KRISTU**

MUTU WALERO: KUKOMANA NDI IMFA WOSAOPA

MAU A M'BUKU LOPATULIKA: Aroma 8:33-39

MAU APAMTIMA: *"Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukakhale inunso."*
*Yohane 14:3*

MTSOGOLERI:

Ndi cifukwa ciani anthu amaopa imfa? (Muyenera kufunsa tsopano funsoli kwa gulu kuti muwathandize kukambirana kuti apereke mayankho pa phunziroli.) Ndi kwa anthu ali onse kukhala wa nkhawa ndi zosadziwika m'moyo uno. Citsanzo ndi ca kukonzekera kupita ulendo wautali pa basi kwa nthawi yoyamba kupita ku ulendo kumene sunapiteko kale. Kodi basi ikafika panthawi yabwino kuti ndikakhoza kukweranso sitima yocokera nthawi iyi? Kodi ndikacita ciani ngati sitima ikandisiya cifukwa palibe inanso kufikira pa Cinayi? Kapena ndicita ciani ngati basi kapena sitina ikaonongeka pa mmseu? Umadera nkhawa ulendo cifukwa siuli kudziwa kuti zidzakhala zotani. Sitidziwa kuti imfa idzakhala yotani. Buku Lopatulika liri ndi ndime zambiri zonena za imfa ndi kunena za moyo itatha imfa kwa amene amakhulupirira mwa Iye.



Ngati munthu akadamwa madzi apacitsimepo adzamvanso ludzu. Koma ngati atamwa madzi amene Yesu apatsa, sadzamvanso ludzu. Akadakwaniritsidwa. Iye anali kulankhula za madzi a moyo amene anali Yesu mwini. Timatenga madzi amenewa tikakhulupirira pa iye. Werengani Yohane 4:14. Munthu amene ali ndi moyo wosatha ali ndi kasupe wa muyayaya. Iye amakwaniritsidwa. Iye sayenera kuthamanga kuno ndi uku kufuna zokondweretsa. Madzi amoyo amathesa ludzu lace. Iye amakhala okhutitsidwa ndi cimwemwe. Ngati ife timwa madzi a moyo, Yesu analonjeza kuti tidzakhala okwaniritsidwa.

GAWO 6: MOYO WOPEREKEDWA NDI MULUNGU

Werengani Yohane 10:28. Ngati munthu wakhulupirira mwa Yesu Kristu, amalonjeza kumusunga iye kwa nthawi zonse. Akunena kuti palibe munthu amene angamukwatule m'manja a Atate ace. Akristu ena amacita mantha pamene acita cinthu coipa. Iwo amaganiza kuti adzataya moyo wosatha wao. Cimeneci ndicosatheka cifukwa Mulungu adzawasunga kunthawi yamuyayaya. Mkristu amafuna kucita cabwino. Amayeretsa kucita bwino. Iye amakhala osakondwa pamene acimwa, cifukwa cimo limasiyanitsa kucoka kwa Mulungu koma ngati anapulumutsidwadi, samataya cipulumutso cace. Limeneli ndi lonjezo la Mulungu. Tikhoza kutsimikiza kuti ndi zoona.

Kutsiriza; pali malonjezo ena a Mulungu a za moyo wosatha:

1. Munthu amene akhulupirira adzakhala ndi moyo wosatha, Yohane 3:16.

GAWO 3: MOYO WOSATHA TSOPANO

Werengani Yohane 3:36. Yesu akuti mu mau amenewa munthu aliyense amene akhulupirira mwa iye "ali nao moyo wosatha." Moyo wosatha umayamba nthawi imene akhulupirira mwa Yesu Kristu. Anthu ena amaganiza kuti moyo wosatha" udzayamba pamene miyoyo yathu idzatha padziko lino, koma cimeneci sicimene Buku Lopatulika limanena. Limanena kuti munthu amene akhulupirira ali ndi moyo wosatha.

Mbali yotsiriza ya mau amenewa kuli lonjezano kwa anthu amene sakhulupirira pa Yesu. Sadzakhala ndi moyo, koma adzakhala ndi mkwiyo wa Mulungu.

GAWO 4: CILENGEDWE CATSOPANO

Werengani 2 Akorinto 5:17. Mulungu analonjeza kuti ngati munthu ali "mwa Kristu," wasanduka olengedwa watsopano. Pamene munthu akhulupirira mwa iye, Buku Lopatulika limanena kuti iye "wabadwanso." Nthawi yoyamba imene munthu anabadwa, anabwera mdziko lapansi ali kakhanda kocepa ali ndi thupi la m'nofu ndi mwazi. Thupi silimakhala locepabe; limakula ndikusintha munjira zambiri. Koma limakhalabe thupi locepa lomwelo. Pamene munthu abadwanso" mwa Yesu Kristu, amabadwa mwa Mzimu. Iye amakhala olengedwa watsopano. Moyo wace wakale wa ucimo umasinthika kucilungamo ca Mulungu.

GAWO 5: MOYO WOKHUTITSA

Yesu analankhula ndi mkazi wocimwa pa citsime. Iye anabwera kudzatunga madzi. Yesu anamuuza kuti akadakhoza kumupatsa madzi amoyo.



GAWO 1: KODI IMFA NDI CIANI?

**Imfa ndi kuti moyo umasiyana ndi thupi. Thupi likafa limakhala lopanda nchito mdziko. Liyenera kutaidwa. Komatu thupi sindiye munthu.** Thupi ndi cinthu cimene munthu amakhalamo ali ndi moyo. Munthu aliyense ndi mzimu amene amakhalabe ndi moyo atafa. Akristu amakhulupirira ndipo amadziwa m'mitima yao kuti imfa ndi khomo limene limawatsogolera kwa Mulungu kukayanjana ndi Iye mu njira yapadera. Motero kodi payenera kukhala mantha a imfa kwa ife eni kapena kwa amene tiwakonda?

GAWO 2: INUYO KUKOMANA NDI IMFA

Anthu ambiri, ngakhale Akristu, safuna kuganiza kapena kulankhula za kufa, koma ndi kanthu kena kamene ife tonse tidzakomana nako, kwa ena pamene ali a ang'ono, ena pomwe ali okalamba. Popeza imfa ndiyoyenera tonsefe, ndiye ndi cinthu cabwino kuti tilingalirepo kweni kweni za imfayi ndi m'mene tiganizira za cimeneci.

Stefano anaponyedwa miyala ndipo anadziwa kuti ali kufa. Kodi iye anakomana nayo motani? Werengani Macitidwe 7:55-60. Kodi Stefano anaopa kufa? Nkhawa yace inali ya pa anthu ena, ngakhale kwa amene anali kumupha.

Kumaoneka kuti ngakhale Paulo anayang'anira nthawi ya imfa yace ndi cimwemwe, cifukwa unali mwai wace wokakhala ndi Kristu. "Pakuti kwa ine kukhala ndi moyo ndiko Kristu, ndi kufa kuli kupindula. Koma ngati kukhala ndi moyo m'thupi, ndipo cipatso ca nchito yanga, sindizindikiranso cimene ndidzasankha. Koma

ndipandidwa nazo ziwirizi, pokhala naco colakalaka ca kucoka kukhala ndi Kristu, ndiko kwabwino koposa-posatu" (Afilipi 1:21-23).

Azibambo awiriwa sanaope imfa cifukwa ca cikhulupiriro cao mwa Mulungu. Iwo anabvomereza ndi kukhulupirira malonjezo a Kristu akuti adzakhala naye. Werengani Yohane 14:1-3.

GAWO 3: KUBVOMEREZA IMFA YA OKONDEDWA

Imfa ya okondedwa imabweretsa cisoni kwa ena a ife amene timatsala cifukwa cimatanthauza kuti sitidzakhala nayenso ameneyu mdziko lino. Kukwiya ndi cinthu cozolowereka ngakhale kukhetsa misozi cifukwa ca cisoni cathu. Ngati amene wamwalirayo ali Mkristu, pamenepo tiyenera kuthokoza Mulungu cifukwa ca citsimikizo cimene anati patsa ife cakuti munthu ali ndi Kristu ku nthawi zonse.

"Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo, wokhulupirira Ine, angakhale amwalira adzakhala ndi moyo; ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakukhulupirira Ine, sadzamwalira nthawi yonse" (Yohane 11:25-26).

GAWO 4: KUNDIZA ENA AIFE MWADZIDZI

Monga Akristu tikhoza kutsogozedwa ndi Mulungu ku banja lomwe lataya okondedwa wace. Nthawi zonse sikwapafupi kucitira umboni pa nthawi yotere. Kwa ena ndi mwambo wawo kudandaula ndi kulira momveka pakakhala maliro. Mkristu akhoza kumva nao cisoni ndi banja lofedwalo wosalowa nao mu mwambo umenewu. Pa nthawi yabwino pamene banja latonthola



GAWO 1: CIFUKWA CIMENE MULUNGU ANATILONJEZERA

Mulungu anatilonjeza malonjezo ambiri kuti tigawane mu zinthu zonse mu banja la Mulungu. Inu munabadwa mu banja. Monga ciwalo ca banja limenelo mwagawana cakudya ca m'banja mo. Mwakhala ndi nyumba yogonamo ndi zobvala, Mwagawana madalitso ndi zitsoni za m'banja. Mwagawananso cikhalidwe ca makolo anu. Mwina nkhope yanu ndiyofanana ndi mai wanu, koma njira zanu ndizofanana ndi atate anu. Komabe mumagawana makhalidwe a banja lanu cifukwa ndinu ciwalo ca banja limenelo. Pamene munakhala Mkristu, munabadwa mu banja la Mulungu. Mulungu anafunanso kuti mugawane mbanja. Amafuna kuti inu mukhale ndimadalitso amene ali operekedwa kwa ana ace. Ndi cotheka kuti inunso mukhozanso kubvutika monga Mwana wa Mulungu Yesu Kristu adacitira. Mulungu anafuna kuti mugawane naye makhalidwe ace, zifukwa zimenezi Iye anatipatsa malonjezano ace ndikuti tikule monga Iye.

GAWO 2: MOYO UMADALIRA PA CIKHULUPIRIRO

Lero taganizira malonjezo ace aza moyo wosatha. Werengani Yohane 3:16. Munthu aliyense amene amakhulupirira mwa Yesu Kristu akhoza kukhala ndi moyo wosatha. Limeneli ndi lonjezo la Mulungu ndipo ndi loona. Iye anapereka mwana wace m'malo mwathu cifukwa anatikonda ife. Iye anatikonda ngakhale kuti tacimwa ndikukhala moyo wosalemekeza dzina lace. Ngati tikhulupirira pa iye, tidzakhala ndi moyo wosatha. Lonjezano limeneli ndi lakwa munthu aliyense amene akhulupirira.

ndi cikondi ca Kristu. Ambuye alemekezedwe.

PHUNZIRO 8

MUTU WAPHUNZIRO: MALONJEZO A MULUNGU

MUTU WALERO: MALONJEZO A MOYO WOSATHA

MAU AMULUNGU: 2 Petro 1:4-11

MAU APAMTIMA: *"Mwa izi adapatsa malonjezo a mtengo wace ndi akulu ndithu; kuti mwa izi mukhale oyanjana nao umulungu wace mutapulumuka ku cibvundi ciri pa dziko lapansi mucilakolako."*
*2 Petro 1:4*

MTSOGOLERI:

Mukacita lonjezano, mumapereka mau anu kuti mudzacita kanthu kena. Mulungu amapereka mau ace kuti adzaticitira zinthu zambiri. Malonjezano ace ndi woona nthawi zonse.

Tikhoza kuwerenga malonjezo ace mu Buku Lopatulika. Koma kungowawerenga sikukwanira. Tiyenera kuwakhulupirira ndi kuwachula kuti akucitikireni ndi kucita kanthu kena poyamba Mai anauza mwana wace ocepa kuti, "ngati uli wabwino, udzalandila kanthu kena kapadera." Mwanayo akadalandira mphatso akadakhala wabwino. Mulungu adalonjeza kwa ife zinthu zina ngati tikhulupirira. Iye amalonjeza za mapemphero, koma poyamba tiyenera kupemphera. Malonjezo a Mulungu a kwa ana ace.



ndi pamene Akristu akhoza kugawana nao za ciyembekezo cao ca mwa Yesu Kristu. Ngati banja lofedwa lija liri la Cikristu akhoza kukhala otonthoza ndi olimbikitsa panthawi ngati imeneyi. Panthawi yocitira umboni monga okhulupirira mwa Kristu, mphamvu zikhoza kubwera ndi madalitso eni eni akhoza kuoneka ngakhale munthawi ya cisoni.

MTSOGOLERI:

Kupyolera mukukambilana kwathu lero tikhoza kuona kuti imfa ndi cinthu comwe tiyenera kukhala naco ndiponso moyo wathu uyembekezera pa dziko lino la pansi. Ngati inu mukuona kuti muli kuopa kufa ndi kuopa kuti banja lanu lifa, yesani kuiganizira ndipo mufike pomvetsetsa cifukwa ca manthawa. Werenganinso ndime za Mau a Mulungu zimene zinena za imfa. Mu ndime zimenezi yang'anani malonjezo a moyo wa mtsogolo. Dzifunseni nokha mafunso awa. Kodi ndi makhulupiriradi mwa Mulungu wa mphamvu zonse? Kodi Mulungu akhozadi kupatsa moyo wosatha? Kodi Kristu anaperekadi moyo wace cifukwa ca ine kuti ndisafere m'macimo? Ngati siudziwa kuyankha mafunsowa, mukhoza kufunsa mbusa wanu kuti alankhule nanu za zimenezi.

Pempherani kuti Mulungu akhoza kucotsa mantha a imfa kucokera m'mitima yathu kuti tikhale naco ciyembekezo cokwana ca moyo wosatha mwa Iye. Tiyeni tione pamodzi ndi Paulo kuti, "Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu ziripo ngakhale zinthu zirikudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale colengedwa cina ciri conse, sicingadzakhoze kutisiyanitsa ife ndi

cikondi ca Mulungu, cimene ciri mwa Kristu Yesu Ambuye wathu.

PHUNZIRO 5

MUTU WAPHUNZIRO: NDICIANI CINGATISIYANITSE IFE NDI CIKONDI CA KRISTU?

MUTU WALERO: ZOKHUMUDWITSA MBANJA CIFUKWA COSABALA ANA KAPENA KUKHALA NDI AMBALI IMODZI.

MAU A M'BUKU LOPATULIKA: Aroma 5:1-5

MAU APAMTIMA: *"Cisomo canga cikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa mufoko."*
*2 Akorinto 12:9*

MTSOGOLERI:

Pamene mwamuna ndi mkazi akonda ndikukwa tilana cinthu coyembekezera ndi ana obadwa mucigwirizanoci. Ana amabweretsa cimwemwe mu banja, ndipo amadziwika kuti ndi madalitso ocokera kwa Mulungu. Koma nanga bwanji ngati ana sabadwa? Kodi cimeneci ciri kutanthauza kuti Mulungu sakonda banja limeneli? Sizotero ai. Kodi zikutanthauza kuti limeneli sibanja leni leni ndikuti pamaso pa Mulungu akhoza kusiyana ndi kukwatiwanso? Pamenepa limeneli sindiye tanthauzo lace. Tiyeni tione ngati tingabvomerezane ndi mlembi waphunziroli.



ni mau a mu Buku Lopatulika apafupi. Imbani nao nyimbo za cikristu. Mudzipita nao ku chalichi ndiku sande sukulu. Adzudzuleni pamene acita colakwa. Aonetseni kuti mumawakonda. Alangeni pamene sanamvere. Pangani kuti banja lanu likhale lokondwa. Zonsezi zidzathandiza mwana kukula ndi kukonda ndi kulemekeza makolo ace monga momwe mwakondera ndi kusamalira iye.

MTSOGOLERI:

Mumaphunziro anai otsatanawa talankhula za mayesero ambiri amene anabwera kwa ife m'moyo. Kodi zimenezi zikhoza kutisiyanitsa ndi cikondi ca Kristu? Osati pamene tipitiriza kuika cikhulupiriro cathu mwa Kristu. Pokambirana kwathu taona m'mene mayesero amenewa akhoza kuonjezera cikhulupiriro cathu ndikutilimbitsa mwa Ambuye. Palibe aliyense angaitane kapena kulandira mokondwa mabvuto otere m'miyoyo yathu, ndipo pamene abwera tiyeni tikule mucikhulupiriro cifukwa ca iwo. Palibe malo aliyonse amene Kristu analonjeza kuti moyo wa Cikristu udzakhala wosabvuta. Iye analonjeza kukhala ndi ife. Mtumwi Paulo anati, "Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale, moyo, ngakhale angelo, ngakhale maufumu, ngakhale zinthu ziripo, ngakhale zinthu zirinkudza, ngakhale zimphamvu, ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale colengedwa cina ciri conse, sicingakhoze kutisiyanitsa ife ndi cikondi ca Mulungu, cimene ciri mwa Kristu Yesu Ambuye wathu" (Aroma 8:38-39). Ngati tiri ndi cikhulupiriro cofanana ndi comwe Mtumwi Paulo anali naco, tikatero ifenso, tikhoza kunena mau omweo ndikuwatanthauzadi, kuti palibe cinthu cimene cingasiyanitse

ndi utsogoleri wa Mulungu kulowetsa ana athu sukulu ndi kulephera mwa izi, tiyenera kuyamika cifukwa ca cidziwitso comwe apeza ndi maphunziro amene alandira. Iwo akhoza kuwerenga akhoza kulemba, ndipo akhoza kuwelengera ciwelengero ca manambala. Ngati titanthandiza kuti tiwapezere mabuku, iwo akhoza kupitiriza kumawerenga, kulemba ndi manambala ndikupiliza kukhala anzeru. Pa malo a ulimi ana akhoza kuphunzira nchito ya ulimi ndipo atsikana akhoza kukondweretsedwa pophika ndi kusoka. Cinthu cofunika koposa ndikuwasunga mowatanganidwitsa ndicidwi cophunzira zinthu zatsopano. Pemphani cithandizo ca Mulungu ndi citsogolero mu zimenezi.

## GAWO LACITATU: ANA ENA AMATAIKA

Ngakhale kuti makolo Acikristu ena aphunzitsa ana ao za cikondi ndi cipulumutso ca mwa Kristu ena amaganiza kuti amadziwa njira bwino, imene ili njira ya dziko. Mu nthano imene Yesu ananena yomwe tikuidziwa ya Mwana wolowelera, Atate sanataye ciyembekezo cakuti mwana wace adzabwerera. Ngakhale mwana amene wakula ndi kusiya nyumba yace monga ngati sakondanso banja lace, sitiyenera kusiya kumukonda ndikupempherera. Timayenera kupitiriza kukonda mwana ngakhale zimene acita sitibvomerezana nazo kapena kukonda zomwe acita.

Monga makolo a ana ocepa tiyenera kuzindikira kuti ana ocepa adzakula ndikukhala ana akulu. Kodi tingawaphunzitse motani kuti atsate njira ya Kristu? Yambani kuwaphunzitsa pamene ali ocepa kwambiri. Auzeni nthano za mu Buku Lopatulika.

Awerengereni Buku Lopatulika. Aphunzitse-



## GAWO 1: UKWATI OPANDA ANA

Pamene ana sabadwa m'nyumba nthawi zonse mumakhala kukhumudwa kwa mkazi ndi mwamuna. Koma ndi ena akazi amatenga pathupi mwamsanga, koma ena amakhala nthawi yaitali. Ndi cinthu cabwino ngati mwamuna ndi mkazi alankhula za zofuna zao pa kubadwa kwa mwana. Kupita ku kliniki ya za dongosolo la kabalidwe kapena kwa sing'anga nthawi zambiri cimathangata kupeza ngati pali bvuto la mthupi. Nthawi zambiri amalangiza kuti mwamuna abwerenso cifukwa kukhala opanda mwana kukhoza kucitika ndi mwamuna kapena mkazi. Pothandizidwa ndi thandizo lamankhwala, ndikupemphera kufunsa Mulungu kuti akudalitseni ndi ana ngati cili cifuniro cace. Kumbukirani mmene Sara ndi Hana a m'Buku Lopatulika anapatsidwa ana patatha zaka zambiri zidikira ndi mapemphero.

## GAWO 2: MADALITSO NGAKHALE OPANDA ANA

Yesu anati, "Cifukwa ca ici mwamuna adzasiya atate wace ndi amai ace, nadzaphatikizana ndi mkazi wace, ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi? Cotero kuti salinso awiri koma thupi limodzi. Cifukwa cace ici cimene Mulungu anacimanga pamodzi, munthu asacilekanitse" (Mateyu 19:5-6).

Masiku ano amuna amayamba kuganiza zotenga mkazi wina ngati oyamba sanamubelekere mwana. Ngakhale kuti iye akonda mkazi wace cikhumbo cofuna mwana cimakhala camphamvu koposa cikondi cace ca pa iye. Cimeneci ndi cosiyana ndi ziphunzitso za Kristu. Iye anati, "Ndipo awiriwo adzakhala mmodzi." Iye sananene kuti, "Ngati atakhala ndi mwana, adzakhala thupi li-

modzi." Mwamuna ndi mkazi ali thupi limodzi, ngakhale kuti abadwe kapena ai. Sipangakhale cokwaniritsa cifukwa cakuti palibe ana, koma Mulungu akhoza kudalitsanso banja limeneli. Mkazi ayenera kuthokoza Mulungu cifukwa ca ciyanjano cao ndi mwamuna wace ndikumupempherera kuti amuthandize kuti akhale mkazi wabwino kwa iye. Mkazi sayenera kunena mwamuna wace ngati ana sabadwa ndiponso mwamuna sayenera kunena mkazi wace.

## GAWO 3: KUBVOMEREZA ZINTHU ZIMENEZO SITINGASINTHE

Masiku ano mu Afrika mabanja opanda ana amatenga ana kuti akhale ao amene alibe makolo kapena makolo amene sakhoza kuthandiza bwino ana ao. Cimeneci cimakhala cothandiza kwambiri kwa iwo ndi kwa ana ngati mwamuna ndi mkazi abvomerezana kucita cimeneci limodzi. Iwo akhoza kutenga khanda limeneli kapena mwana ndikumukonda monga mwana wao weni weni. Koma ngakhale sangacite kapena kutenga mwana wa ena kukhala wao, awiriwa akhoza kulemekezedwabe ndikukhala ogwiritsidwa nchito m'mudziwo ndi mu mpingo. Cimeneci sicotheka ngakhale kuti angokhala kunyumba ndikukhala mwa kukhumudwitsa kwao cifukwa, cosakhala ndi ana. Ngati iwo acita izi ndikuyamba kudzimvera cisoni okha, sangakhale okondwa ndipo sangakwaniritse cifuniro ca Mulungu ca miyoyo yao.

Mkristu wina wa cimai wabwino kwambiri amene analibe ana anafotokoza mwamene iye anafunira kukhala ndi ana mu nyumba yace Iye anati pa zaka zoyamba za ukwati wao iye ndi mwamuna wace anali kudikira ndi kuyembekezera ana. Iye anali kulila misozi kwambiri cifukwa panalibe comwe cinaoneka. Ndipo iye anati anapempha Mulungu kuti agwiritse nchito moyo wace



ana anu mphatso zabwino, kopambana kotani nanga Atate wanu wa kumwamba adzapatsa zinthu zabwino kwa iwo akupempha iye? (Mateyu 7:7-11). Motero ngati tikhulupirira kuti Mulungu amatikonda ndikutisamalira ife, tidzapemphera kumufunsa kuti atipatse zosowa zathu. Ndipo ndikukhulupirira kwa thunthu mwa iye kucicita. Cimeneci sicitanthauza kuti tingokhala pansi ndi kudikira pa Mulungu kuti atigwetsere cakudya pamaso pathu cili pambale cokonzeka kale kuti cidyedwe. Ai tiyenera kucita zomwe tingakhoze kucita kuti tikwaniritse zosowa za pa banja lathu. Ine monga mkazi ndi bambo, tikhoza kupeza nchito kuti ithandize zosowa za pabanja lathu. Kapena banja likhoza kufuna kubwerera kukakhala kumudzi kufikira mwamuna atapeza nchito ina. Mulungu akhoza ndipo adzatitsogolera mu nthawi yonga imeneyi; ngati titangomukhulupirira iye ndi kudikira iye kuti ationetse zomwe tiyenera kucita..

## GAWO 4: MAPHUNZIRO A ANA ATHU NDI OFUNIKA KOPOSA

Makolo onse a Cikristu amafuna kuona ana ao ataphunzira bwino. Cimeneci ndi cinthu ca bwino ndipo ife monga makolo tiyenera kucita zonse zomwe tingakhoze kuwathandiza kuti apeze maphunziro. Komatu cimeneci sindico cinthu cofunika koposa ndi cowaphunzitsa njira ya Kristu. Ndizoonadi, tikhoza kucita zimenezo ndikuwathandizabe kuti aphunzire sukulu. Sicinthu cotheka kuti ana onse atsirize giledi seveni, ndi kufika ku sekondale, kuti akhoza kupita ku sukulu ya pamwamba Yunivesite. Ana onse sakhala ndi nzeru zokwanira kuti akhoze kutsiliza maphunziro amenewa. Ndiponso kulibe sukulu zokwanira zomwe ana onse akhoza kucita zimenezi. Ngati titacita kucita potsogozedwa

MTSOGOLERI:

M'maphunziro athu amwezi umo tirikuganiza za zinthu zomwe nthawi zina zimayesa kufooketsa cikhulupiriro cathu ndikusiyanitsa kucikondi ca Kristu. M'miyoyo yathu muli mabvuto ambiri-mbiri mayesero ndi zokhumudwitsa. Ife monga Akristu, tiyenera kulimbikira kuti tikhale Akristu olimba cifukwa ca zimenezi m'malo mofuna kuzilora kuti zitisiyanitse kucokera kucikondi ca Kristu. Kodi ife tingacite zimenezi bwanji?

GAWO 1: ZINTHU ZONSE ZICOKERA KWA MULUNGU

Pamene mwamuna monga bambo acotsedwa nchito cimeneci cimabweretsa mabvuto ambiri ku banja lonse lathunthu. Mu midzi ndi mumizinda ikulu ikulu kodi cakudya cikhoza kumacokera kuti? Kodi ndalama za lendi adzipereka bwanji? Ndalama zolipirira sukulu? Ndi zinthu zina zambiri? Mulungu anadziwa ndikusamalira zinthu zonsezi zomwe zimatibvuta ife. Kodi tikhoza kukhulupirira zosowa kuti Mulungu azisamalire ndikudalira pa Iye? Paulo anati, "ndipo kwa Iye amene angathe kucita koposa posatu zonse zimene tizipempha, kapena tiziganiza, monga mwa mphamvu ya kucita mwa ife" (Afeso 3:20). Iye anali kunena za Mulungu amene ali ndi mphamvu zonse ndi wacikondi. Yesu anati, "pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu, funani, ndipo mudzapeza, gogodani ndipo cidzasegulidwa kwa inu pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citsegulidwa. Kapena munthu ndani wa inu, amene popempha mwana wace mkate, adzapatsa mwala? Kapena popempha nsomba, adzapatsa iye njoka kodi? Comweco, ngati inu, muli oipa, mudziwa kupatsa



mu Utumiki wace. Umboni wace ndiwakuti Mulungu anamutsogolera kusukulu ya mu Mzinda wace kukaphunzitsa Mau a Mulungu cinthu comwe anacita kwazaka zambiri. Munjira imeneyi iye anathandiza anyamata ndi atsikana ambiri kuti adziwe Kristu monga Mpulumutsi ndi Ambuye wa miyoyo yao. Iye anati mu njira imeneyi anali ndi ana mazana m'malo mokhala ndi ana owerengeka. Banja la Cikristu lao linali banja la ana a sukulu amene anali kutali ndi kumidzi ya mabanja ao.

Banja lopanda ana liyenera kubvomereza kusowa kwa mwana kwao, osati temberero, koma monga kaitanidwe. Iwo ayenera kucitenga cotsogozedwa ndi Mulungu. Mulungu anawasankhula iwo mwapadera ndi colinga cofuna kuti akwaniritse bwino pamene alibe ana a iwo okha. Ngati cimeneci ciri cifuniro ca Mulungu, adzawadalitsa opanda malire.

GAWO LACINAI: KUKHALA NDI ANA ACINYAMATA KAPENA ATSIKANA OKHA

Amuna ambiri ndi akazi ena amafuna kuti ana ao akhale anyamata ndi atsikana, osati anyamata okha ndipo cimakhala cabwino pamene ali ndi onse, koma ngati muli ndi anyamata okha kapena atsikana, pamenepo musaiwale kuthokoza Mulungu cifukwa ca iwo ndi cifukwa ca madalitso ace akukuonetsani inu. Kondani aliyense poyankha pa yekha ndipo dziwani kuti Mulungu ali ndi colinga pa moyo umenewo.

Cofunika koposa ndico kupemphera kwa Mulungu kukuthandizani ndi mwamuna wanu kuti mukhale makolo abwino. Pemphani Mulungu kuti akutsogolereleni kuphunzitsa za m'Buku

Lopatulika ndi m'mene iwo ayenera kudzitsatirira moyo wao onse.

MTSOGOLERI:

Mtumwi Paulo ananena kuti palibe cinthu cina mu cilengedwe conse cimene cingatisiyanitse kucokera kucikondi ca Kristu, ngakhale zokhumutsidwa cifukwa cosakhala ndi ana. Mulungu ndi wabwino kwa ife potipatsa moyo, thanzi, nyumba, cakudya, cikondi, cipulumutso ndi madalitso ena ambiri amene sitingakhoze kuwachula. Cimatikakamiza tonsefe kupitiriza iye cifukwa ca madalitso amenewa koposa kuganizira za zimene tiribe ndikumaganizira kuti tiyenera kukhala nazo.



munthu wopundukayo mwina comwe anacifuna kucokera kwa ife ndi cikondi kudera nkhawa koposa ena amene ali bwino.

MTSOGOLERI:

Kupyolera mu phunziroli lero takumbutsidwanso kuti m'mayesero aliwonse a moyo tiyenera kuzindikira kuti ndi madalitso angati a moyo, cimwemwe, mtendere ndi cisangalalo cifukwa ca cikondi cace m'mitima yathu. (Patsani ena mwai wochula madalitso ena). Tiyeni tipemphe Mulungu kuti atitsogolere m'mayesero a moyo ndikuti phunzitsa kuti tidzidalira pa iye kwambiri. Funsani Mulungu kuti atithandize kuti tikule mwa iye cifukwa ca mayesero amenewa.

## PHUNZIRO 7

MUTU WAPHUNZIRO: KODI NDI CIANI CINGATISIYANITSE IFE NDICIKONDI CA KRISTU

MUTU WAPHUNZIRO WALERO: KUKOMANA NDI ZOKHUMUDWITSA NDI CIKHULUPIRIRO (KUTHA KWA NCHITO? KUSOWEKA KWA MAPHUNZIRO A ANA, KUTAIKA KWA MWANA.)

MAU AMULUNGU: Mateyu 6:25-33

MAU APAMTIMA: *"Idzani kuno kwa Ine nonsenu akulema ndi akuthodwa, ndipo Ine ndidzakupulumutsani inu."*
*Mateyu 11:28*

M'mawa wina tsiku la sabata mu mpingo wa Baptist pamene mbusa anali kulalikira, m'nyamata wina wa zaka khumi ndi ziwiri anayamba kubvutika ndimatenda ace akhunyu. Pambali imene anakhalayo anthu anayamba kucokapo kumusiya m'nyamatayo yekha kotero kuti akanagwa pansi ndikudzipweteka. Potsiliza munthu wina yemwe anakhala mbari ina anafika ndikumuthandiza za kuti apite panja komwe akanakagona pansi. Cikanakhala cinthu cabwino ngati anthu amene anakhala naye pafupi akanathandiza mwamsanga m'malo moyamba kusokoneza pomasuntha.

Khunyu ndi matenda, ndipo munthu amene ali ndi matendawa sayenera kuopedwa koposa munthu amene ali ndi malungo ayenera kuopedwa. Ngati munthu aopa, kawiri kawiri ndi cifukwa cosamvetsetsa. Iye monga Akristu, tiyenera kuphunzira za zimene sitimvetsetsa kuti tikhoze kukhala osaopa ndi kuthawa kupangitsa odwalawo kuti akhumudwe cifukwa ca matendawo.

GAWO 4: YESU ANAGWIDWA CIFUNDO PA IWO

Mu mauthenga timaona zitsanzo za Yesu pamene anakomana ndi anthu amene anali ndi mabvuto ofanana. Mu nthawi ili yonse Yesu anali ndi cikondi ndi kugwidwa cifundo cifukwa ca iwo, ndipo anawaciritsa. Ife tiyenera kutsata citsanzo ca Yesu. Ndizoonadi tiribe mphamvu yociritsa, koma ife tikhoza kukonda ndikupereka thandizo.

Nthawi zambiri mbanja mwana amene ali osiyana ndi anzace cifukwa ca mabvuto kapena kupunduka sakondedwa ndikusamalidwa mofanana ndi ana ena. Nthawi zina banja limakhumudwa cifukwa ca bvuto limeneli. Mwana kapena



PHUNZIRO 6

MUTU WAPHUNZIRO: KODI NDICIANI CINGATISIYANITSE IFE KUCIKONDI CA KRISTU

MUTU WALERO: KUIMA MOLIMBIKA MCIKHULUPIRIRO KUPYOLERA MMABVUTO (MONGA NGATI MOYO WOFOKA? KUKHALA NDI MWANA WOFOOKA? MATENDA APA THUPI, KHUNYU, KUSOKONEKERA KWA MUTU)

MAU AMULUNGU: Aroma 12:1-2

MAU APAMTIMA: *"Si kuti ndinena monga mwa cipewero, pakuti ndaphunzira ine, kuti zindikwanire ziri zonse ndiri nazo."*
*(Afilipi 4:11)*

MTSOGOLERI:

Tonse amene tiri ndi matupi a thanzi timaziyesa zinthu wamba osaganizira kwambiri kuti ndimadalitso amenewa. Ife amene tiri ndi moyo wabwino nthawi zambiri timabvutikira zinthu zing'ono zing'ono za moyo monga kusakhala ndi zinthu zonse tikuzifuna, monga ndalama zambiri zobvala, nyumba yabwino, wailesi, galimoto, television ndi zinthu zina. Pamene mayesero amenewa abwera kwa ife monga moyo wofoka, matenda, mwana wosakhwima, kusowa luntha, khunyu kapena kusokonekera kwa mutu kwa ife kapena m'modzi wa pa banja lathu, kodi timacita motani kwa iwo? Monga Akristu kodi tiyenera kucita motani kwa iwo? Kodi cikhulupiriro cathu cimakhalabe colimba kapena timayamba kukaikira kuti Mulungu alibe ndi malonjezo ace kwa ife? Padakali pano tiyeni aliyense wa ife

aganizire za cimeneci ndikuziyankhira mafunsowa tokha.

GAWO 1: KUBVOMEREZA MAYESO MWACIKHULUPIRIRO

Werengani Afilipi 4:11-13. Pamene mayesero a moyo abwera kwa ife, ngakhale amtundu otani, tiyenera kuwabvomereza mwacikhulupiriro. Tiyeni tikumbukire Yobu ndi mayesero ambiri mbiri anali nao, komabe iye anali wokhulupirika kwa Mulungu. Tiyenera kukhulupirira zimenezi m'matenda kuti Atate wathu wa Kumwamba adzakhala nafe kaya ticira mwamsanga kapena ndi matenda amene tiyenera kupirira kwa kanthawi. Mtumwi Paulo anati, "pakuti ndaphunzira ine, kuti zindikwanire ziri zonse ndiri nazo." Kodi Paulo anali kuti pamene analema mau amenewa? Iye anali ku Aroma m'ndende, koma iye sanali osakondwa. Iye anabvomereza kuti anagwidwa ndipo anali kudera nkhawa zakucitira umboni kwa asilikali amene anali kulonda akaidi ndi kulemba makalata ndikuthandiza abwenzi ace ku Afilipi. Ngati mutawerenga kalata yonse ya Afilipi, mudzaona kuti pali nthawi zambiri zomwe analemba za kukondwera ndi cikondwerero cake mwa Ambuye. Paulo anakhoza kubvomereza ndikukhala okondwa mnyengo yace cifukwa ca cikhulupiriro cace mwa Ambuye. Iye anapereka moyo wace mwa iye podziwa kuti sangamukane koma kuti akhala naye.

GAWO 2: KUKONDWERA MMASAUTSO ATHU MWA CIKHULUPIRIRO

Sicinthu copusa kunena kuti tiyenera kukondwera ngakhale m'masautso athu. Paulo mu Aroma 65:3-5 amanena kuti "Ndipo cotero cokha, komanso tikondwera m'zisautso; podziwa ife kuti cisautso cicita cipiriro; ndi cipiriro cicita cizolowezi, ndi cizolowezi cicita ciyembekezo: ndipo ciyembekezo sicicititsa manyazi, cifukwa cikondi ca Mulungu cinatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife."

Pakakhala matenda kapena mabvuto ena, sikunena kuti tiyenera kuwabvomereza ndikumangokondwera osaona asing'anga kapena osatsata malangizo azi dotolo ndithandizo tingalipeze. Sitiyenera kutero. Tiyenera kugwiritsa nchito nzeru zonse zimene Mulungu anatipatsa kuti tibweretsa mtendere kwa ife ndi banja lathu. Mkazi amene ali mu Buku Lopatulika yemwe anali ndi nthenda yakukha mwazi kwa zaka makumi awiri anakhala akupita kwa a sing'anga ambiri mbiri ndipo sanakhale bwino. Iye anakhala ndicikhulupiriro cakuti ngati atangokhudza cobvala ca Yesu adzaciritsidwa. Yesu anati kwa iye, "mwana wamkaziwe, cikhulupiriro cako cakupulumutsa; muka mumtendere, nukhale wocira cibvutiko cako" (Marko 5:34).

GAWO 3: KUKONDA NDIKUTHANDIZA ENA KUPYOLERA M'MABVUTO

Masiku ano tikamayenda Mzinda kapena kupyolera m'mudzi tikhoza kuona opunduka, kapena amene ali osautsidwa m'njira ina, amene ali ndi khunyu, amene tikhoza kukhala naye wina wace mu banja amene ali ndimabvuto amenewa, kapena kuzemba kumanena za iwo kuti akhoza kumva? Kapena kodi timayesetsa kumva mabvuto ao ndikuyesa kuwathandiza?